

KODI CIDZAKHALA KUTI CIMALIZIRO CANU?



Okonedwa moyo, ngati mutafa lero lino, kodi *mukudziwa* ngati mudzapita kumwamba kapena ku gehena kukakhala nthawi zonse? Baibulo, Mawu a Mulungu, akuti mukhoza kudziwa.

Bwenzi langa, ndikukufunsani funso lofunika kopambana pa moyo wanu wonse. Yankho lanu linganene za kumene mudzakhala nthawi zonse! Funso ndi lakuti: **Mudapulumsidwa inuyo?** Funso silakuti ngati ndinu membala wa mpingo, koma inu mudapulumsidwa? Sindikunena kuti muli ndi moyo wabwino, koma mudapulumsidwa?

Sindikuti mukucigwirira ntchito, kapena kuti mukuyembekezera koteru, koma mudapulumsidwa? Baibulo likuti, “...*tiyenera kupulumutsidwa.*” (Macitidwe 4:12).

Kuti mupulumutsidwe, bvomerezani kuti ndinu wocimwa. “*monga kwalembedwa, Palibe mmodzi wolungama, inde palibe mmodzi...Palibe mmodzi wakucita zabwino, inde, palibe mmodzi ndithu.*” (Aroma 3:10, 12). “*pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu;*” (Aroma 3:23). Mnzanga, macimo anu akukupangitsani kukhala operewera mu ulemerero wa Mulungu, ndipo simungathe kukumana ndi zokuyenerezani zake kuti mudzapite kumwamba.

Zindikirani kuti wina wake adakukondani nakuferani inu. Yesu adafa pamtanda kuti alipire macimo anu ndi kukupatsani mwayi wakupita kumwamba. “*Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha m’menemo, kuti pokhala ife cikhaliro ocimwa, Kristu adatifera ife.*” (Aroma 5:8). Pamene Yesu adafa pa mtanda, mwazi wake udalipilira mphotho ya macimo anu. “*Mwa Iye amene tiri nao maomboledwe mwa mwazi wake, ngakhale cikhululukrio ca macimo;*” (Akolose 1:14).

Zindikirani kuti simungapange cina cili conse kuti mulandire kapena kupeza citandizo cokuyenerezani ulendo wanu wakumwamba. Yesu adatha kulipililatu pamene Iye adafa pa mtanda. Iye asadafe adati, “***Kwatha;***” (Yohane 19:30). Tsopano iye akufuna “kukupatsani” malo ku mwamba. “...*mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu.*” (Aroma 6:23).

Zindikirani kuti pamene Yesu wakupulumutsani inu cidzakhala kwa muyaya. Yesu sadakhale wakufa. Iye adauka m’manda, ndipo tsopano ali moyo kumwamba kupitiliza kupembedzera za iwo amene

akhulupilira mwa Iye. *“Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenenso ndinalandira, kuti Kristu anafera zoipa zathu, monga mwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kuti anaukitsidwa tsiku lacitatu, monga mwa malembo.”* (1 Akorinto 15:3,4). *“kucokera komweko akhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa Iye, popeza ali nao moyo wace cikhaliro wa kuwapembedzera iwo.”* (Ahebri 7:25).

Mwachikhulupiliro mulandireni Yesu Khristu. Yesu adafa kudzapereka mphatso ya moyo wosatha kwa munthu aliyense. Koma monga mphatso zina zonse, iyi singakhale yaphindu pokhapokha mutailandila mwa inu nokha. *“Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lace.”* (Yohane 1:12). Cikhulupiliro ndiko kukhulupilira mwatunthu. Baibulo likunena kuti: *“inu mwapulumutsidwa mwa cikhulupiliro,”* popanda inu kuonjezerapo kanthu kalikonse. *“Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera kutchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense.”* (Aefeso 2:8,9). Chikhulupiliro chopulumutsa ndi chokhacho chokhulupilira mwa Yesu Khristu mwatunthu. *“Ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka,”* (Machitidwe 16:31). Cina cili conse cimene mumayesa kuonjeza pa cikhulupiriro ndi "ntchito". *“Pakuti timuyesa munthu wolungama cifukwa ca cikhulupiliro wopanda ntchito za lamulo.”* (Aroma 3:28).

Okondedwa moyo, ngati mukufunitsitsa kuleka njira yanu, ndi kumukhulupilira mwatunthu Yesu Kristu, ndipo tsopano lino mukhoza kupulumuka! Tsopano ziri kwa inu! Mungoweramitsa mutu wanu

ndipo mupemphere kwa Mulungu ndi mawu anu ndi kudzipereka kwa iye kuti ndinu ochimwa oyenera kukhala kugehena, koma ndi mtima wanu wonse, mukukhulupilira Yesu Kristu kuti akupulumutseni inu kuchokera kugehena ndi kusintha njira ya moyo wanu. Baibulo likuti, *“kuti ngati udzabvomereza m’kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka ...pakuti, amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka.”* (Roma 10:9, 13).

Ngati simunabvomereze kulakwa kwanu ndikhulupirira Yesu Kristu ngati Mpulumutsi wanu, conde werengani zimene Baibulo limanena: *“...wosakhulupira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu.”* (Yohane 3:18) Conde musakane Uthenga Wabwino! Khulupirani Kristu lero!

Conde tuma traki lino kwa ife kuti tidziwe ngati wasankha kukhulupirira Yesu Kristu kukhala Mpulumutsi wako utawerenga trakili.

Dzina _____

Keyala _____

Zaka _____

Foni _____



FELLOWSHIP TRACT LEAGUE

P.O. BOX 164 • LEBANON, OH 45036

www.fellowshiptractleague.org © Tract 8073 (Chichewa)

All tracts free as the Lord provides. Not to be sold.